



**Kufalitsa Nkhani: Wailesi ndi Wailesi ya Kanema
(Media Radio and Television)**



International
Labour
Organization

TIMVERENI

Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana

Kulimbikitsa Ufulu wa Ana Kudzera M'maphunziro, Zaluso
ndi Njira zofalitsira Mauthenga



TIMVERENI

Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana

**Kulimbikitsa Ufulu wa Ana Kudzera M'maphunziro,
Zaluso ndi Njira zofalitsira Mauthenga**

**Kufalitsa nkhani:
Wailesi ndi Wailesi ya Kanema**

Kabukuka ndi kamodzi ka mabuku a maphunziro a TIMVERENI Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana. TIMVERENI ndi maphunziro olimbikitsa ufulu wa ana kudzera m'maphunziro, zaluso ndi njira zofalitsira mauthenga. Mabukuwa analembedwa mu chaka cha 2011 ngati mbali imodzi ya pulojekiti ya IPEC/ILO ndi chithandizo chochokera ku boma la Italy.

IPEC/ILO ikulimbikitsa kuti mabukuwa ayikidwe mu zilankhulo zosiyanasiyana komanso kusindikizidwanso kuti ntchito yothetsa m'chitidwe ogwiritsa ntchito ana ipite patsogolo. Ngati mwatanthauzira bukuli mu chinenero china kapena kusinthako mbali ina ya mabukuwa, kumbukirani kunena komwe mwatenga uthengawo ndiponso mutumizireko a ILO/IPEC mabuku kapena mbali yomwe mwasintha.

TIMVERENI– Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana. Kulimbikitsa ufulu wa ana kudzera m'maphunziro, zaluso ndi njira zofalitsira mauthenga, Ntchito Yolimbana ndi Khalidwe Logwiritsa Ntchito Ana pa dziko lonse,

International Programme on the Elimination of Child Labour (IPEC), International Labour Office (ILO), Geneva, 2011.

ISBN N. 92-2-113 240-4

Mungathe kudziwa zambiri za TIMVERENI kuchokera ku:

International Programme on the Elimination of Child Labour (IPEC)
International Labour Organisation (ILO)

4, Route des Morillons, CH-1211 Geneva 22, Switzerland
Telephone: +41 22 799 77 47
Fax: +41 22 799 81 81
Email: childlabour@ilo.org
Web site: www.ilo.org/scream

Cholinga: Kukhazikitsa ubale ndi ofalitsa nkhani ndi cholinga chakuti athandize kudziwitsa anthu zakuipa kolemba ntchito ana. Kumvetsetsa momwe ofalitsa nkhani amagwilira ntchito. Kukonzekera komanso kuyankha mafunso pa nkhani yolembe ntchito ana pa wailesi ndi wailesi zakanema.



Phindu: Zimalimbikitsa mphamvu zopezeka kudzera mu kuphunzitsa anthu zakuipa kolemba ntchito ana komanso momwe anthu ochepa omwe amva uthenga angaphunzitsire anthu ena ambiri.

Nthawi

Maphunziro awiri alimodzilimodzi ndi limodzi lophatikizana

Chilimbikitso

Chigawochi chidzakudziwitsani kusiyana kofalitsa nkhani kudzera mu manyuzipepala ndi kufalitsa nkhani kudzera pa wailesi kapena pa wailesi ya kanema. Tikukhulupilira kuti poyamba chigawo ichi mwaphunzitsa kale chigawo cha nyuzipepa ndi kuti achinyamata a gulu lanu akudziwa kufunika kogwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana zofalitsira nkhani pofuna kudziwitsa anthu ambiri za zimene iwo akuchita.



Zigawo zonse zofalitsa nkhani zikuunika momwe achinyamatawa angagwiritsire ntchito ofalitsa nkhani pofuna kudziwitsa anthu za zomwe akuchita ndi momwe anthuwa angawathandizire. Zigawozi zikulumikizana bwino ndi zigawo zina monga Kulemba Nkhani Mopeka komanso Chofufuzafuza ndi Kuyankha Mafunso.

Ubwino waukulu wazigawo zofalitsa nkhanizi ndi wakuti zimapereka mpata kwa achinyamatawa kuti agwiritse ntchito zimene akhala akuphunzira. Ndi njira ina yowathandizira kuti akule mumaganizidwe ndi machitidwe azinthu pamene akupatsidwa maudundo osiyanasiyana.

Kudzera mu zigawozi achinyamatawa aphunzira luso logwilira ntchito ndi ofalitsa nkhani makamaka masiku ano pamene nkhani zikukhala zofunika kwambiri pa miyoyo ya anthu. Luso limeneli lidzawathandiza munjira zambiri pa moyo wawo wam'tsogolo, ku sukulu komanso kuntchito.



Chidziwitso

Yesetsani kuphunzitsa chigawo Chofalitsa Nkhani mu Nyuzipepa musanaphunzitse chigawo ichi. Chigawo chofalitsa nkhani kudzera mu nyuzipepa chiwathandiza achinyamatawa kulimbikitsa chikhulupiliro chawo pogwira ntchito ndi ofalitsa nkhani. Nthawi zina achinyamata amatha kubisa anthu amene alemba zofalitsa zawo pamene apereka uthenga wawo kudzera mu nyuzipepa koma sangachite izi poyankha mafunso pawalesi kapena pa wailesi ya kanema. Ubwino woyambira chigawo chofalitsa mauthenga kudzera ku manyuzipepala musanaphunzitse chigawo ichi ndi wakuti achinyamatawa akhonza kugwiritsa ntchito kalata yachidziwitso imene analemba muchigawocho pofuna kuyambitsa ubale wawo ndi ofalitsa nkhani pa wailesi kapena wailesi yakanema.

Kukonzekera

Musanayambe kuphunzitsa chigawo ichi ganiziranipo kaye zinthu izi:

Ndi wailesi kapena wailesi ya kanema iti imene ingakhale yoyenera pofalitsa uthenga wathu? Wailesi ndi wailesi ya kanema zaboma zikhonza kukhala zabwino pofalitsa uthenga wanu chifukwa sizifuna kuti mulipire polengezetsa uthenga wanu wa mtundu uwu. Komabe wailesi zina za anthu zikhonzanso kukuthandizani. Pamene mwasankha wailesi yoti ifalitse uthenga wanu, onani bwino pa mapologalamu amene amaulutsidwa ndipo musankhe amene ali oyenera kuti mulengezetsemo mauthenga anu.

- **Lankhulani ndi ogwira ntchito ku wailesizi nthawi isanakwane.** Ogwira ntchito ku wailesi ndi wailesi ya kanema amafunika kuuzidwiratu kuti muwatumizira kalata yanu yachidziwitso ndipo muyenera kuwauza kuti kalatayi ikukamba za chiyani. Anthuwa nthawi zambiri amakonzeratu mapologalamu a sabata lonse, choncho powadziwitsa mwamsanga zakalata yanu angathe kukuuzani za nthawi imene ingadzaulutsidwe.
- **Kuchita zinthu pa nthawi yoyenera.** Ndibwino kukamba za zinthu zimene zikuchitika tsopano osati zimene zinachitika masabata a mbuyomu. Muyenera kukonzekera bwino kwambiri pa nkhanu ya nthawi yopangira chigawo ichi, makamaka inu, aphunzitsi.
- **Nthawi yotseka.** Onetsetsani kuti ogwira ntchito kuwailesi kapena wailesi ya kanema alandira kalata yanu yachidziwitso panthawi yoyenera ndipo lankhulanani ndi mkozi wa pologalamu imene idzaulutse kalata yanu kuti akuuzeni za nthawi imene adzakufuneni kuti mukayankhe mafunso okhudzana ndi kalata yanu pawailesiyo.

Ogwira ntchito ku wailesi ndi wailesi ya kanema amakhala otanganidwa kwambiri. Choncho njira yabwino yoti muwathandizire kuti nkhanu yanu iwulutsidwe ndi kuyesetsa kugwira ina mwa ntchito imene amayenera kuchita. Ngati mutalemba kalata yanu yachidziwitso momveka bwino zidzawathandiza ogwira ntchitowa kuti awone poyambira pa nthawi yokufunsani mafunso ndikuchita nawo zokambirana. Mukalemba kalatayi mukhonzza kutsatirapo polankhula ndi ogwira ntchitowa pa zimene mwalembazo. Ngati mwagwira bwino yambiri mwa ntchito yawo ndikulankhula nawo momveka bwino pa za kalatayo, mudzachelukitsa mwayi wanu woti kalatayi iwulutsidwe.

Ngati mukudziwa wina aliyense amene anagwirako ntchito yofalitsa mawu pawailesi kapena ku wailesi ya kanema ndipo ndiwokonzeka kukuthandizani pa nthawi iyi, mupempheni kuti atero. Mwinanso n'kutheka kuti mukudziwa wina amene amagwira ntchito yofalitsa mawu ku wailesi kapena ku wailesi ya kanema mufunseni otereyu ngati angakuthandizeni. Mutakhala ndi mwayi, a wailesi kapena wailesi yakanema akhonzza kutumiza munthu wawo kuti adzakuthandizeni pa chigawo ichi. Mwinanso akhonzza kukhala omasuka kubwera ndi kudzalankhula ndi gulu lanu pa momwe olemba nkhanu amagwilira ntchito ndi zomwe mungachite kuti olemba nkhanu adzitha kukumana nanu pafupipafupi kuti alembe nkhanu zanu. Achinyamata nthawi zambiri amakondwa akamamva momwe olemba nkhanu amagwilira ntchito ndipo nthawi zambiri amamvetsera mwachidwi.



Thandizo lapadera

Njira inanso yopezera thandizo lapaderali ndikukumana ndi katswiri pa ntchito. Ngati simukudziwa wina aliyense wa akatswiriwa, mukhonza kupeza maina awo mu buku la ma nambala a telefoni. Poganizira za mtundu wa ntchito imene muli nayo, mukhonza kuwafunsa akatswiriwa ngati angathe kukuthandizani mwaulere.

Kuti achinyamatawa aphunzire kwenikweni zimene ayenera kuchita, atumeni kuti afunefune anthu amene angathe kuwaphunzitsa zokhudza chigawo ichi. Alimbikitseni ndikuwathandiza pa momwe angakumanirane ndi akonzi ndi ena ogwira ntchito ku wailesi kapena wailesi yakanema. Ndinjira yabwino yowapangitsa kuti akhale ndi chidziwitso chenicheni cha momwe zinthu zimakhala pogwira ntchito ndi ofalitsa nkhani. Kalata iliyonse yachidziwitso yopita ku nyumba yofalitsa mau iyenera kutsatiridwa ndi kulankhulana pa telefoni ndi amene akuyenera kuyilandira.

Zofunikira

- ✓ Kalata imene inalembedwa muchigawo chofalitsa mauthenga kudzera ku nyuzipepa.
- ✓ Bolodi loyera/lakuda kapena mapepala olembapo pophunzitsa.
- ✓ Telefoni, koma sichofunika kwenikweni.
- ✓ Chojambulira (video camera), ndi kanema.



(Chidziwitso): Tikudziwa kuti zina mwazipangizo tatchulazi ndi za mtengo wokwera kwambiri ndipo sizingapezeke m'madera onse. Zigwiritseni ntchito pokhapokha ngati muli nazo).



Kuyamba



Momwe mungayambire kuphunzitsa chigawo ichi, zidalira zinthu zina zingapo monga:

- Ngati mwakwanitsa kapena ayi kubweretsa munthuwakunja kuti adzukuthandizeni.
- Ngati muli ndi mphunzitsi mnzanu woti akuthandizeni pophunzitsa chigawo ichi.
- Ngati muphunzitse chigawochi nokha.

Chidziwitso

Ndibwino kuti mugwiritse kaye ntchito imodzi ya njira zofalitsira mauzi muchigawo ichi: wailesi kapena wailesi yakanema. Ngati mutafuna mukhonza kulifunsa gulu lanu kuti lisankhe kuchita chigawo choyerekeza kutenga mbali ya munthu wina muzochitika za pa wailesi kapena wailesi ya kanema. Mudzaona kuti maguluwa adzakonzekera mosiyana kutengera ngati akachite zochitika zawo pa wailesi ya kanema kapena pa wailesi.

Njira yophunzitsira mene yafotokozedwa m'musiyi ndiyokwanira kukuthandizani mosatengera mafunso atatu ali m'mwambawa ngakhale mutakhala kuti simunaphunzitseko chigawo ngati ichi.

Kukonza gulu

Poti chigawo ichi chikubwera pambuyo pa chigawo chofalitsa mauthenga kudzera ku manyuzipepala, ndibwino kuti timagulu tating'ono timene munakhazikitsa tija tisaphwanyidwe. Ntchito ina ya muchigawo chino ndiyofanana ndi yomwe achinyamatawa anagwira muchigawo chofalitsa mauthenga kudzera ku manyuzipepala. Muchigawo chino achinyamatawa aonjezerapo chigawo choyerekeza kutenga malo amunthu wina poyankha mafunso pa wailesi ndi wailesi ya kanema. Zochitikazi zidzawapatsa chikhulupiliro mwa iwo eni asanakumane ndi ofalitsa nkhani.

Ngati mwaphunzitsa kale chigawo choyerekeza kutenga malo a munthu wina kapena cha mtsutso, muyenera kuti mukudziwa achinyamata odziwa kulankhula kugulu la anthu ndikuchita bwino zisudzo. Onetsetsani kuti oterewa asakhale mugulu limodzi; agawidwe ndi cholinga chakuti luso lawo lithandize ena. Mukhonza kuwasankha kukhala atsogoleri amagulu enawa.



Kukonza zonse zoyenera

Phunziro limodzi

Ngati munakwanitsa kupeza munthu wochokera ku wailesi kapena pa wailesi ya kanema, mu itaneni kuti adzalankhule ndi gulu lanu musanayambe kuphunzitsa. Izi zikhonza kubweretsa chidwi chachikulu mwa achinyamata anu popeza adzadziwa kuti alowadi muchigawo chokhudza anthu ofalitsa mauthenga. Lolani kuti pakhale kufunsa ndikuyankha mafunso kumapeto a zimene munthu wakunjayu walankhula. Mukhoza kukhala oyamba kufunsa mafunso kuti achinyamatawa amasuke. Zindikirani kuti achinyamata nthawi zina amachita manyazi kuti ayambe kufunsa mafunso ngakhale atakhala nawo ambiri.

Mlendoyu akabwelera kwawo, onetsetsani kuti mwalemba kalata yomuthokoza mwamsanga. Kuthokoza kotere ndi ulemu wapadela komanso kumathandiza kuti munthuyu adzakhale omasuka kubweranso ngati mutamupemphanso m'tsogolo.

Ngati simunathe kuitana mlendo wakunja, onetsetsani kuti mwakhazikitsa zonse m'malo munjira yoti achinyamatawa awone kuti akulowa muchigawo chofalitsa mau.

Kawirikawiri achinyamata amakonda kanema kwambiri kuposa wailesi makamaka chifukwa chakuti kanema imatha kuonetsa nthawi yomweyo zithunzi za momwe zinthu zikuchitikira. Choncho achinyamata amamanga mfundo zoyendetsera moyo wawo kuchokera ku zimene amawonera pa mapulogalamu a pa kanema Ndichifukwa chake mapulogalamu ambiri a pa kanema amapangidwa ndi cholinga chosangalatsa achinyamata. Ngakhale kuti izi zili chonchi ku maiko ena, wailesi ndi omwe ili ndi chikoka chambiri kuposa kanema ndipo yenera kugwiritsidwa ntchito moyenera.



Wailesi ili ndi ubwino wambiri woposa wailesi ya kanema poti ndiyotsika mtengo ndipo siivuta kupeza. Ubwino wina ndiwakuti anthu amatha kumvera wailesi kwa tsiku lonse, sabata yonse ndi kwa chaka chonse. Nthawi zambiri amamvera wailesi asakuzindikira konse poti imakhala ngati mbali imodzi yazochitika za moyo wawo. Ubwino wina ndiwakuti imapezeka mu nyumba zambiri ndi kumalo ogwilira ntchito. Komanso kumaiko kumene magetsi sanafike m'dziko lonse komanso kumene anthu ambiri ndiwosaphunzira, ngati kwathu kuno, anthu sangathe kukhala ndi wailesi ya kanema. Kumalo otere wailesi ndi chida choyamba chomvelera nkhani mwamsanga, komanso chosangalatsira anthu.



Wailesi ndi kanema zimakhala ndi mapulogalamu osiyanasiyana ena okhudza azimayi, ena achinyamata, ena a maphunziro, ena omva maganizo a anthu kudzera ku matelefoni ndi ena otere. Inu ndi gulu lanu muyenera kusankha pulogalamu imene zochitika zake zingagwirizane ndizochitika za pulojekiti yanu. Kawirikawiri achinyamata amakonda kumvera kapena kuonera mapulogalamu amene apangidwa kuti asangalatse gulu lawo monga okhudza nyimbo, masewero a moyo wachinyamata ndi opereka maganizo awo kudzera ku matelefoni.

Ngati ku dela lanu kuli wailesi yomveka kudela lokhalo, muyenera kuzindikira kuti anthu amakonda kwambiri wailesi zotere kuposa wailesi zomveka dziko lonse chifukwa wailesi zoterezi zimafulutsa mozama nkhani zimene zikukhudza anthu a kudalalo. Ngati wailesi zotere ziliko ku dela lanu, zikhonza kukhala bwino kuyambira kulumikizana ndi ofalitsa nkhani. Ubwino wina ndiwakuti ogwira ntchito ku mawailesi otere amakhala akufunafuna nkhani zoti afulutse.

Zochitika zoyamba: Kuyankha mafunso pawalesi kapena pa television

Zigawo ziwiri zophunzira

Chimodzi mwa zinthu zomwe zimapangitsa kanema kukhala yopambana ndipamene anthu ayankha mafunso pawalesiyi. Chigawo ichi chakonzedwa ndicholinga chofuna kuphunzitsa achinyamata momwe angayankhire mafunso pawalesi yakanema. Zotsatira za muchigawo chofalitsankhani kudzera ku nyuzipepa zikhala chiyambi cha zochitika za muchigawo chino. Gulu lililonse likhale ndi kalata imene linalimba ndipo liyerekeze kuti kalatayo inapita ku nyumba yofalitsa mau, wailesi kapena wailesi ya kanema. Cholinga chathu pano chikhala chakuti achinyamatawa aphunzire kuyerekeza kuti atenga malo a munthu wina pamene magulu awo ang'onoang'ono akhale akuunika bwino kalata zimene analemba. Ayenera kupeza mafunso kuchokera ku makalatawa ndipo mafunsowa afunsidwe kwa amene akutenga mbali pa pulojekitiyi ndipo ayenera kupeza mayankho a mafunsowa.



Chidziwitso

Sikoyenera kwenikweni kuti chigawo choyerekeza kutenga malo a munthu wina chiphunzitsidwe kaye musanayambe chigawo ichi. Dela lofunika kuyerekeza kuti munthu watenga malo a wina muchigawo chino silalikulu kwambiri pofaninizira ndi dela lenileni loyerekeza kuti munthu watenga malo a wina, limene limabwera lisanabwere la Zisudzo. Choncho musade nkhawa ndi kuchepa kwa luso lopangira zisudzo muchigawo chino.

Njira zofunsira ndi kuyankhira mafunso

Poyamba kambiranani ndi gulu lonse. Lembani pa bolodi malamulo awa pokonzekera kuyankha kapena kufunsa mafunso pa wailesi kapena kanema:

- **Konzekerani** Kuyankha mafunso kwamtundu uliwonse kumapereka theng'eneng'e ngakhale kwa amene anazolowera kuyankha mafunso otere. Pokonzekera kuyankha mafunso mumathandiza gulu lanu kuti likhazikitse mitima pansi ndikuchoka mantha komanso kuti maganizo awo akhazikike pauthenga umene akufuna kupereka.

- Fikani panthawi yoyenera.** Nthawi zambiri anthu odzayankha mafunso amadikilira ku maofesi a wailesi kapena wailesi ya kanema. Mukaphonya nthawi yanu kumakhala kovuta kuti akupatseninsu ina. Kufika mwamsanga kumathandiza achinyamatawa kuti akhazikike asanayambe kulankhula pawailesi kapena wailesi ya kanema.
- Nkhani yanu ndiyotani.?** Kutu kuyankha mafunso kwanu kukhale koyenera kuulutsidwa pa wailesi kapena wailesi ya kanema kukuyenera kukhala kofotokoza nkhanu. Cholinga chanu ndikugwira chidwi cha omvetsera choncho muyenera kuganiza pamene mukulankhula.
- Auzeni kuti inu ndinu ndani.** Ndikofunika kuti omvera adziwe amene akulankhula kuti athe kulumikiza bwino zimene mukunena.
- Lankhulani ndi ziganizo zapafupi komanso zofupika** Osalankhula mozungulira pamene mukulankhula pa wailesi. Lankhulani momveka bwino. Osataya nthawi ndikukamba zimodzimodzi pa mfundo imene mwakamba kale.
- Osagwiritsa ntchito mau amene amagwiritsa ntchito akatswiri (jargon) ndi mau a achinyamata (slang).** Ngati mulankhula zimene omvera sakutha kumva amaleka kumvetsera. Achinyamata amakonda kukhala ndi Chichewa chawo chawo choti akuluakulu sangamve. Aphunzitseni kulankhula moti aliyense amve.
- Ganizani za uthenga umene mukufuna kuti anthu amve.** Kuyankha kwabwino kwa mafunso kumadziwika ngati mwakwanitsa kupereka uthenga umene mumafuna kupereka. Choncho ndibwino kukonzekera bwino. Lembani mfundo pafupifupi zisanu zimene mukufuna kunena pa nthawi yoyankha mafunso ndipo onetsetsani kuti mwazifotokoza. Imodzi mwa mfundozi ikhale yothokoza anthu amene ayenera kuthokozedwa. Chofunika kwambiri apa ndikutanthauzira mafunso mwanjira yoti akupatseni mpata onena zimene mukuyenera kunena. Ngati mukulankhula bwino simungayembekezere kuti akudulani mawu pamene mukulankhula.
- Phatikizani umboni wodziwika bwino.** Pali umboni wambili wochitsa nkhanu pa nkhanu yogwiritsa ana ntchito umene mukhonzika kugwiritsa ntchito polimbikitsa mfundo zanu. Kuyankha mafunso pawailesi kumatenga mphindi zochepa chabe ndipo njira yabwino yogwilira chidwi cha omvera ndi kugwiritsa ntchito umboni wotere. Fotokozani za umboniwu poufanizira ndi moyo wa tsiku ndi tsiku ndicholinga chakuti anthu athe kulingalira bwino zimene mukunena.





- **Zindikirani kuti anthu akukuonani.** Pamene mukuyankha mafunso pa wailesi ya kanema muyenera kuganizira bwino za momwe mukuonekera ndikuchitira. Anthu amakuonani kuyambira pachiyambi mpaka pamapeto, choncho mmene mukugwiritsira ntchito thupi lanu ndichinthu chothandiza kwambiri. Achinyamata achenjezedwe kuti asamagwire pakamwa, kapena kuyang'ana kumbali pamene akuyankha mafunso pa wailesi ya kanema. Ayenera awoneke omasuka ndipo manja ndi thupi lawo zikhale zomasuka.

Konzani mfundo zapamwambazi mundondomeko imene mukuona kuti ikugwirizana ndi gulu lanu. Simfundo zonsezi zimene zingakhale zofunika kugulu lanu, choncho sankhani ndikukambirana zokhazo zimene zingakuthandizeni. Kambiranani mfundozi imodziimodzi popereka zitsanzo za zomwe mukutanthauza.

Aloleni achinyamatawa kufunsa mafunso pamene mukupitilira ndi zokambirana zanu. Pomaliza afunseni mafunso kuti mutsimikize kuti amvadi. Mukhonza kugwira chidwi chawo posakaniza mafunso ndi zimene mukuwafotokozera komanso popereka zitsanzo.

Kukonzekera kuyankha mafunso

Cholinga cha dela lino ndichakuti achinyamata a m'magulu ang'onoang'ono athe kuyerekeza kuti atenga malo amunthu wina poyankha mafunso a pa wailesi. Tikufuna kuti gululi lithe kufunsa komanso kuyankha mafunso. Ayikeni maguluwa mu magulu ocholuka oti chiwerengero chawo chikhoza kugawika ndi 2. Keneka akakhale awiriawiri. Magulu awiriwa agwira ntchito zosiyana:

- Gulu loyamba likhala ngati latenga malo a ofunsa mafunso lochokera nyumba yolutsa mau. Aunike bwino kalata yachidziwitso yomwe alandira ndipo apeze mafunso oti akhonza kufunsa. Musawafunse zambiri poopa kuti angaone ngati kuti ntchitoyi ndiyovuta kwambiri. Afunseni kuti apeze mafunso pafupifupi asanu ndi limodzi. Aphunzitsidwe kuti mafunso afunsidwe munjira yakuti ofunsidwayo akhale ndi mpata wolongosola mfundo zake poyankha.

Ayenera auzidwe kuti mayankho achidule monga “inde” “ayi” amachotsa chidwi cha omvera.

- Gulu lachiwiri ligwire ntchito ya ofunsidwa mafunso. Nawonso ayenera aunike mozama kalata yachidziwitso poyang'ana madela ena. Ayang'ane madela a uthenga umene akufuna kupereka pa nthawi yoyankha mafunsoyi.

Magulu amene akhala awiriawiriwa asaonetsane zimene akonza. Cholinga cha zochitika izi ndikulimbikitsa achinyamatawa kuti aganizire za mafunso amene ofunsa mafunso angawafunse ndi momwe iwo angayankhile. Kudzera muzochitikazi, achinyamatawa adzaphunzitsidwa momwe wina aliyense wa iwo angachitire ngati ataitanidwa ku nyumba yawalesi kapena wailesi ya kanema kuti atenge nawo mbali poyankha mafunso. Izi zikhonzanso kulimbikitsa achinyamatawa kuganizira mozama pa za pulojekiti yawo ndi nkhani yogwiritsa ntchito ana.

Perekani mphindi makumi awiri ku gulu lilonse kuti likonzekere. Ngati muona kuti gulu lina likuvutika, lithandizeni pokhala nalo kwa kanthawi pang'ono. Mukhonza kuwapangira mafunso oyambilira ngati kutakhala koyenera kutero. Kawirikawiri zimakhala zovuta kupeza funso loyamba.



Zungulirani m'magulu onse kuti muone ngati zonse zikuyenda bwino. Atsimikizileni kuti pa nthawi ino simukufuna maganizo akuthwa kwambiri koma kuti gulu lililonse lilembe mafunso awo ndipo lakonzeka kukayankha mafunso. Onetsetsani kuti aliyense wa mumagulu ang'onoang'onowa akupereka maganizo ake.

Onetsetsani kuti maguluwa asunga nthawi imene munawapatsa. Thetsani zochitikazi ngakhale zitakhala kuti ena sanamalize.

Kuyankha mafunso moyesera

Khazikani achinyamatawa m'magulu awiri: gulu lofunsa ndi lofunsidwa mafunso, ndipo ngati mwayi watebulo ulipo akhale moyang'anana. Gwiritsani ntchito njira imene gululi lingagwirizane nayo pofuna kusankha momwe magulu ang'onoang'onowa alowere m'bwalo pofunsa ndikufunsana mafunso. Ngati muli ndi chojambulila filimu (video camera), iyi ndi nthawi yoti mukhonza kuigwiritsa ntchito; jambulani zochitikazi. Pobwereza zimene mukujambula, mukhonza kuona momwe mfundo munalemba pa bolodi zija zikugwiritsidwira ntchito. Mukhonza kuwathandiza achinyamatawa powakumbutsa zoyenera ndi zosayenera kuchita panthawiyoyankha mafunso.

Kujambula zochitikazi kumapangitsa achinyamatawa kukhala ndi mantha pakati pawo. Izi ndizothandiza pazifukwa izi:

- Zimapangitsa zochitikazi kukhala ngati zenizeni. Pamene mukufunsidwa mafunso izi ndi zimene zimachitika choncho uwu umakhala mwayi wanu woti mumve momwe zimakhallira nthawi yeniyeni ikakwana dipo mumatha kuona momwe mungachitire.
- Zimapangitsa kuti muyambe kumva momwe zimakhallira mukamaoneka pa kanema pamene mumaonedwa ndi anthu osati amene mukuwaona okha komanso ena amene simukuwaona.

Patsani aliyense mwayi woti ajambule zochitikazi kuti aphunzire momwe angajambulire ndi kuti adzathe kujambula okha gawo loyerekeza kuti munthu watenga malo awina.

Musade nkhawa ngati mulibe chojamburirachi; chofunika ndichakuti gulu lanu lonse latengako mbali ndikuti laphunzira. Ngati mungakhale ndi mwayi wokhala ndi makaseti omvera ndichojambulira chake mukhonza kujambula. Mukhonza kubwereza zimene mwajambulazo kuti amene anatenga mbali pofunsa ndi kuyankha mafunso aone zomwe achita ndi kuti inuyo muthe kufotokoza zomwe munaona. Ndi njira yabwino yophunzilira pamene achinyamatawa amvera zimene analankhula.



Khazikitsani magulu awiriwa moyang'anana pa tebulo ndipo aliyense azindikire mbali imene akutenga. Pofuna kuti athemantha, auzeni kuti ayesere kulankhula monga momwe muulutsi wotchuka yemwe akumudziwa amalankhulira; izi achitendiamene atenga malo a ofunsa mafunso. Ofunsa mafunso ayenera kugawana zimene achite; pasapezeke munthu mmodzi wolankhula yekha. Chimodzimodzi kwa ofunsidwa mafunso, aliyense atenge mbali pofunsidwa mafunso.



Auzeni ofunsa mafunso kuti alimbikitse oyankha mafunso kufotokoza mfundo zawo ngati akufuna kufotokoza bwino funso kapena mafunso amene anafunsidwa poyamba. Izi ziyenera kulimbikitsidwa poti ndi momwe zimakhulira pa nthawi yoyankha mafunso pa wailesi. Akumbutseni oyankha mafunso kuti akumbukire uthenga umene akufuna kupereka ndikuti aupereke pamene akuyankha mafunso.

Onetsetsani kuti achinyamatawa akusangalala ndipo mukhonza kuwathandiza kuti amasuke powapangitsa zinthuzina zomwe zingawasangalatse. Musatalikire pamene achinyamatawa akuyankha mafunso pakuti nthawi zina ena amatha kusokonekera ndikusowa chonena pa nthawi yofunika kwambiri. Athandizeni ngati zitafika potere.

Pamene gulu lililonse latha kuyankha mafunso awo, athokozeni ndipo funsani amnzawo otsala kuti anene maganizo awo pa zomwe amene amaliza achita. Ndibwino kuti enawa aphunzire pa zimene amnzawo achita ndipo agwiritse ntchito maphunzirowa pamene nthawi yawo yakwana. Muyenera kulemba ndikusunga zabwino ndi zoipa zomwe mwakhala mukuona ndicholinga chakuti mukazikambirane pa nthawi ya zokambirana zomaliza. Yesetsani kuwalimbikitsa achinyamatawa pa zabwino zimene achita ndipo aphunzitseni mowaunikira zoyenera kuchita pa madera amene sanachite bwino.

Ngati mwaona kuti ndikoyenera, chititsani mpikisano pakati pawo. Izi zikhonza kuwapangitsa kuti akhale ndi chidwi ndi zomwe akuchita komanso zikhonza kuwasangalatsa. Mukhonza kupereka mphoto kwa:

- Amene achita bwino pa gawo lotenga malo a ena (gulu lonse ndi limene lisankhe opambana).
- Amene aseketse anthu kwambiri potenga mbali za ena.

Kuyankha mafunso

Pamene mwatsiriza chigawo choyesererachi, uzani gulu lanu kuti likonzekere zopita ku nyumba yaulutsira mau kapena wailesi ya kanema. Ndizosatheka kuti aliyense apite nawo ku malowo. Mkozi wa mapulogalamu ya wailesi kapena wailesi ya kanema amafuna inu, ngati oyang'anira gululi, kuti mukhaleko. Poopa kukhumudwitsa ena mwa achinyamatawa, ndibwino kusankha opita nawo pogwiritsa ntchito njira imeme aliyense angagwirizane nayo. Imodzi mwa njirazi ndiyochita maere. Alimbikitseni amene alephera kupita nawo kuti asade nkhwawa poti mwayi wina udzapezeka mtsogolo.

Pamene mwauzidwa za tsiku ndi nthawi yokayankha mafunso, kumanani nawonso achinyamatawa ndikuwathandiza kuti akhazikitse mitima yawo pansi. Akumbutseni zimene munawaphunzitsa pa nthawi imene munakumana ndi gulu lonse lija pazoyenera ndi zosayenera kuchita. Akumbutseni uthenga umene akufuna kupereka. Fikani ku maofesi a wailesi kapena wailesi ya kanema mwa msanga. Zikatha zonse ayenera kuthokoza amene amawafunsa mafunso. Akatha kuyankha mafunso, asabalalike nthawi yomweyo. Ngati mungathe, akonzereni zakumwa kuti amasuke ndikusangalala kuti aiwaleko za nthumanzi imene inawagwira panthawi yoyankha mafunso.

Ngati a wailesi kapena wailesi ya kanema sangathe kukupatsa makaseti amene ajambula zimene achinyamatawa amachita, onetsetsani kuti mmodzi wa iwo ajambule zimene zikuchitika.

Athokozeni pa ntchito imene agwira ndipo musankhe mmodzi wa iwo kuti alembe kalata yothokoza ku wailesi kapena wailesi ya kanema. Muyenera kulimbikitsa ubale umene mwakhazikitsa ndi a wailesi kapena wailesi ya kanema.

Zoyenera kuchita ndi zoyenera kupewa

- Onetsetsani kuti aliyense akutengako mbali pazochitika za chigawo ichi.
- Musalole gulu lina kuchepetsa ntchito imene gulu lina lachita. Magulu onse ayenera kupatsidwa ulemu.
- Sungani makanema kapena makaseti omvera ngati munajambula.
- Ngati ena mwa achinyamatawa sakumasuka ndi zochitika zina za muchigawo ichi, musawaumilize kuchita zimene sakufuna kapena sangathe; ena sangathe kulankhula ku gulu.
- Musalimbikire kwambiri mipikisano ngati njira yofuna ukwaniritsa zolinga za chigawo ichi. Nthawi zina mipikisano yotere imasokoneza umodzi wa gulu.



Kukambirana komaliza

Phunziro limodzi

Pamene aliyense watengako mbali pa gawo lake khala nawoni pansiyachinyamata onsewa. Achinyamatawa ayenera kukhala okondwa kwambiri ngati anali ndi mpata oyankha mafunso pa wailesi kapena wailesi ya kanema chifukwa azindikira kuti anthu awaona pa kanema kapena kuti amva mau awoa wailesi ndikuti anthuwo azindikira zimene akuchita. Muyenera kusunga makaseti azimene munajambula pa nthawi yoyankha mafunso kuti mudzazigwiritse ntchito pa nthawi yofuna kumva maganizo achinyamatawa pa nthawi imene zonsezatha.

Auzeni achinyamatawa zimene anthu a ku wailesi ya kanema kapena wailesi zina akunena pa zomwe iwo achita. Ngati wailesi ya kanema kapena wailesi imenemu na lankhulapo ndi yomveka dziko lonse, uwu ukhonza kukhala mwayi wanu woti pulojekitiyanu idziwike dziko lonse. Muyenera kutsatira pa zinthu zina zimene ofalitsa nkhani angafune kudziwa zokhudza pulojekiti yanu.



Kuunika momwe ntchito yayendera ndi kuchita kalondolondo.

Pali zinthu zingapo zimene zingakuthandizeni kudziwa ngati mwaphunzitsa bwino chigawo ichi. Zina mwa izo ndi zakuti pomaliza pachigawochi achinyamata akhale atatengako mbali pa chigawo chotenga malo a munthu wina poyankha mafunso pa wailesi kapena pa wailesi ya kanema. Ubwino wa momwe achitire izi udzadalira kwambiri momwe mwakwaniritsira kuphunzitsa chigawochi ndi ubale womwe ulipo pakati pa achinyamatawa.

Zizindikiro zina ndi:

- Ngati mwatha kukhazikitsa ubale ndi ofalitsa nkhani pawailesi kapena pa wailesi ya kanema.
- Ngati mwatha kutumiza kalata yachidziwitso kwa ofalitsa nkhani.
- Ngati munapatsidwa mwayi woyankha mafunso pa wailesi kapena pa wailesi ya kanema kapena konseku.
- Ngati simunakayankhe mafunso, mwina munatengako mbali pa pulogalamu zina za pa wailesi kapena pa kanema komwe mwatha kupereka uthenga wanu.
- Ngati mwatha kuyambitsa ntchito yoti itsatilidwe pogwira limodzi ndi ofalitsa nkhani potsatila kuyankha mafunso.

Cholinga cha chigawo ichi ndichakuti achinyamata ayambe kuchitapo kanthu pa nkondo yolimbana ndi kugwiritsa ntchito ana. Zizindikiro zimene zafotokozedwa pamwambazi zikuthandizani kuona momwe achinyamatawa atsimikizira zotengapo mbali pa nkhanayi. Zotsatira za zochitikazi ndizofunika kwa inu podziyesa nokha za momwe mwaphunzitsira chigawo ichi. Pofika tsopano muyenera kukhala mutadziwa achinyamata amene ali odzipereka pa ntchito ya pulojekitiyi.

Chigawo ichi ndichofunika kwambiri pa maphunziro a achinyamatawa. Zochitika za muchigawochi ziwaonetsa momwe angachitire pofuna kuphunzitsa anthu za vuto logwiritsa ntchito ana. Akhonza kuonetsa maganizo awo kwa anthu ena onse. Uthenga wawo ungathe kupita kumalo kwina kumene iwo sangakudziwe.



Anthu ndi magulu ena akhoza kuyamba kukhala ndi chidwi ndipo mwina akhonza kuyamba kufuna kulankhula nanu. Kupereka uthenga kwa ofalitsa nkhani kukhonza kukhala njira yabwino yotsekulira makomo ena.

Chigawochi chikulimbikitsa uthenga wachilimbikitso. Achinyamatawa ayamba kuona kuti zonse sizinaipiretu ndipo kuti iwo akhonza kuchitapo kanthu. Ngati chigawochi chaphunzitsidwa bwino chikhonza kubweretsa zotsatira zopambana.

Pamene mwatsiriza chigawo ichi pitani ku chigawo china. Tikukupemphani kuti chigawo chinachi chikhale chowathandiza achinyamatawa kudziwa njira zina zolimbanirana ndi mchitidwe wogwiritsa ntchito ana, monga kugwiritsa ntchito anthu ena.



Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana

ILO
International programme on the
Elimination of Child Labour (IPEC)

ILO/ IPEC Malawi Project
Mantino Complex
Behind Bizonowaty filling station
PO BOX 30135
Lilongwe

Tel: (+265)-0- 1 770 388/ 199/155

www.ilo.org/ipec

ISBN 92-2-113240-4

